Mulanje Cedar akusoweka thandizo lathu

Kwa nthawi yaitali anthu ambiri amakhulupilira kuti Mulanje Cedar ndi chozizwa chochokera kwa Chauta. Kotero palibe nzeru ya munthu imene ingathe kuteteza mitengoyi kuti isathe mphiri kaamba kakuti Cedar sadzalidwa.
Koma kafukufuku watsimikiza kuti Cedar wambiri yemwe agwiritsidwa ntchito lero anadzalidwa kalekale. Mwachitsanzo, misitu ina ya Sombani, Chambe, Lichenya ndi Fortlister inachita kudzalidwa.
Cedar wina anakadzalidwanso ku Zomba ndi ku Chikangawa ndipo anachita bwino. Kotero nzotheka kubwedzeletsa mtengowu.

Ngati mukufuna kudziwa zambiri;

Mulanje Mountain Conservation Trust
P.O. Box 139,
Mualanje, MALAWI

Tel: +265 (0) 1 466 282/179
Fax: +265 (0) 1 466 241

E-mail: info@mountmulanje.org.mw
Website: www.bgci.org

Ndondomekoyi ikuyendetsedwa ndi Nthambi ya za Nkhalango, Botanic Gardens Conservation International komanso Mulanje Mountain Conservation Trust ndi thandizo lochokera ku U.K. kudzera ku Department for International Development (DfID)

SAVE OUR CEDAR

MALAWI'S NATIONAL TREE

Mulanje Sida, Mtengo wa fuko la Malawi

Mulanje Cedar/Sida/Nkungudza ndi mtengo omwe umapezeka m'Phiri la Mulanje kokha mdziko la Malawi. Kuchokera ku mtengo umenewu anthu amatha kucheka matabwa abwino komanso olimba, osadyeka ndi chiswe. Umathanso kugwiritsidwa posema ziboliboli.

Phindu la mtengowu lapangitsa kuti anthu azingodula mwachisawawa kotero kuti pano mitengo ya Cedar yatsalamo yochepa kwambiri m'phirimu. Kuwonongeka kwa Cedar ndi mitengo ina kwadzetsa kusowa kwa chuma kwa anthu ozungulira nkhalangoyi kukokoloka kwa nthaka komanso kusefukira kwa madzi chifukwa chakuti madzi amabwera ambiri komanso mothamanga kuchokera mphirimu nyengo yamvula ikafika.

Mtengowu uli pachiopsezo kwambiri. Ngati njira zina zotetezera kapena kubwezeretsa mtengowu sizipezeka, mtengowu udzasoweratu.

Ndondomeko ya ntchito yosamalira Cedaryi, ndi chikonzero chopangidwa mothandizana ndi Nthambi ya za Nkhalango, a za kafukufuku, amabungwe, ndi anthu ozungulira nkhalango ya Phiri Mulanje ndi cholinga chodzalanso ndi kubwezeretsa chiwerengero cha mitengo ya Cedar mu nkhalangoyi. Mgwirizano wa magulu amenewa udzakhala ndi phindu lokhalitsa kwa mtengo wa Cedar komanso anthu ozungulira Phiri la Mulanje.

Malinga ndindondomeko ya ntchitoyi, Phiri lidzayezedwa kuona kuti mitengo ya Cedar ili malo ati komanso kupeza malo abwino oyenera kudzala mitengoyi.

Anthu ozungulira nkhalangoyi adzaphunzitsidwa njira zofesera komanso zopezera phindu ndipo adzathandizidwa kuti nawo apange ma Nazale awo a mitengoyi.

M'mbuyomu chikonzero chodzala mitengo ya Cedar sichinapindule kwambiri, pa zifukwa zosiyanasiyana komabe mitengo ya Mulanje Cedar imakula bwino mu nkhalango ya Phiri la Mulanje komanso madera ena monga ku Zomba. Mu chikonzero chapano muli akatswiri oona za mitengo yosiyanasiyana kuti athandize kuunikira ndi cholinga choti zotsatira zake zikhale zopambana.

Kuphatikiza pa kubwezeretsa mitengo imeneyi m'Phiri la Mulanje, ntchitoyi ichitikanso m'madera ena kuti Mulanje Cedar azithanso kudzalidwa kumeneko. Ntchito imeneyi ithandizanso kuti mbande za Cedar zikhale ndi msika waukulu komanso kuti chiwerengero cha mtengowu chisatheretu komanso kuti anthu ofesa akhale ndi njira yokhazikika yopezera ndalama.